# PHUNZIRO LA 65

1. Kodi Yesu anabwera pa dziko la pansi ndi cholinga chakuti ife tidzimutumikira Iye kapena kuti tidzitsata njira yathuyathu yopitira kumwamba?
-Ayi.

2. Kodi khungu la Batumeyu, likutikumbutsa ife chiyani za anthu onse?
-Anthu onse anabadwa ndi khungu ngati Batumeyu.

3. Kodi anthu onse anabadwa bwanji ndi khungu?
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, anasanduka kukhala a khungu ku zowona zen-izeni za Mulungu.

4. Kodi Batumeyu anakatha kupanga china chilichonse kuti achotse khungu lache?
-Ayi.

5. Kodi anthu akhoza kutha kupanga china chakwe kuti achotse khungu lawo kuti athe kuwona zowona zenizeni za Mulungu?
-Ayi.

6. Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kupelera kuwona kwa Batumeyu?
-Yesu.

7. Kodi ndi ndani yekha amene angathe kupereka kuwona kwa anthu onse?
-Yesu.

8. Kodi chifukwa chiyani Batumeyu anamutcha Yesu Mwana wa Davide?

-Chifukwa chakuti Yesu anali chidzukulu cha Mfumu Davide chimene Mulungu analonjeza kuti chidzakhala Mpulumutsi.

9. Kodi chifukwa chiyani anthu anamuletsa Batumeyu kumuyitana Yesu pomuwuza kuti akhale chete?
-Anthu ankaganiza kuti Yesu sankafuna kuchiza munthu wa khungu ndipo opempha wa umphaŵi.

10. Kodi Yesu sankafuna kuti amuthandize munthu wa khungu ndipo opempha wa umphaŵi?
-Ayi.

11. Kodi Mulungu amakonda munthu wina aliyense ndikufuna kumupulumutsa?
-Inde.

12. Kodi Yesu anamubwezera Batumeyu kuwona kwache?
-Inde.

13. Kodi Yesu ankapita ku Yelusalemu kukaŵapulumutsa anthu ku ulamuliro wa Aloma?
-Ayi.

14. Kodi chifukwa chiyani Yesu anapita ku Yelusaremu?
-Yesu anapita kukaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Chifukwa chakuti Atsogoleri a Ayuda ankamuda Yesu, anafuna njira yakuti amuphere Iye.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:1-2

1-Tsopano patatsala masiku aŵiri kuti phwando la



-Yesu analankhulanso kuti mpesawo ndi chizindikiro cha magazi Ache.

-Kodi nanga mpesa ukhala bwanji chizindikiro cha magazi a Yesu?
-Magazi a Yesu adzaturutsidwa ngati m'mene unkaturutsidwira mpesawo kuchokera mu chikho kuti umwedwe.

-Kodi Yesu analankhula kuti mwazi wache ukhetsedwera yani?
-Yesu analankhula kuti mwazi wache akhetsedwa chifukwa cha anthu ambiri.

-Atatha kudya, Yesu analankhulanso kwa ophunzira ache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:25-26

25-[Yesu anati] “Ine ndikukuwuzani zowona, Ine sindidzamwanso chipatso cha mpesa, kufikira patsiku lijalo, limene ndidzamwa icho chatsopano mu Ufumu wa Mulungu.”
26-Ndipo atayimba nyimbo, anaturuka napita ku phiri la Azitona.

-Anali madzulo amene Yesu anamaliza kudya pamodzi ndi ophunzira ache.

-Atatha kudya chakudya chawo, Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anachoka mu Yerusalemu, ndikupita ku phiri la Azitona.

-Yudasi adzalangidwa mpaka kalekale chifukwa cho-mupereka Yesu.

-Iwo akudyabe, Yesu analankhulanso kwa ophunzira ache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:22

22-Ndipo pamene iwo anali kudya, Yesu anatenga mkate, nawudalitsa, nawunyema, nawupereka kwa ophunzira ache, nati, “Idyani; ili ndiye thupi langa.”

-Yesu anatenga mkate naŵadalitsa Ambuye Mulungu, nawunyemanyema, nawupereka kwa ophunzira ache.

-Yesu analankhula kuti mkatewo ndi chizindikiro cha thupi Lache.

-Kodi mkatewo unali bwanji chizindikiro cha thupi la Yesu?
-Thupi la Yesu lidzanyemedwa ndi anthu oyipa ngati m’mene Iye ananyemelanyemela mkatewo.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:23-24

23-Ndipo kenako [Yesu] anatenga chikho, na-chiyamika, nachipereka kwa iwo, ndipo onse anamwa kuchokera mwa icho.
24-Ndiponso anati kwa iwo, “Ichi ndi mwazi wanga wa chipangano umene udzakhetsedwe chifukwa cha ambiri.”

-Kenako Yesu anatenga chikho cha mpesa, naŵayami-ka Ambuye Mulungu, nachipereka kwa ophunzira a che.



Pasaka ndi mikate yopanda chofufumitsa lichitike, aku-luakulu amsembe ndi aphunzitsi a malamulo anafunafu-na njira yimuchitira chiwembu Yesu ndi kumupha.
2-Iwo anati, “Koma lisakhale tsiku la phwando la Pasaka, ayi, pakuti pangakhale phokoso la anthu.”

-Kodi chifukwa chiyani Atsogoleri a Ayuda sanafune ku-mugwira Yesu pa tsiku la Pasaka?
-Chifukwa chakuti iwo ankadziŵa kuti akamugwira Yesu pa tsiku la Pasaka, anthu aŵawukira iwo.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:10

10-Ndipo Yudasi Isikariyote, m’modzi wa khumi ndi aŵiriwo, anachoka napita kwa akuluakulu amsembe kuti akampereke Yesu kwa iwo.

-Kodi Yudasi anali ndani?
-Yudasi anali m’modzi mwa ophunzira khumi ndi aŵiri amene Yesu anaŵasankha.

-Kodi Yudasi ankadziŵa kuti iye anabadwira mu tchimo, ndipo akufunika Yesu kwa iye ngati Mpulumutsi wache?
-Ayi.

-Kodi Yudasi ankakhulupilira kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi?
-Ayi.

-Yudasi sanamutsatire Yesu chifukwa chakuti iye sankakhulupilira kuti Yesu anali Mpulumutsi.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Yudasi ankamutsatira Yesu?
-Yudasi ankamutsatira Yesu chifukwa chakuti ankafuna

kuti apeze ndalama zambiri.

-Chifukwa chakuti Yudasi sanapeze ndalama kwa Yesu, iye anaganiza zomupereka Yesu kwa adani ache.

-Kodi amene anamutsogolera Yudasi kuti amupereke Yesu anali ndani?
-Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Satana anafuna kuti Yudasi amupereke Yesu?
-Chifukwa chakuti Satana amamuda Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani Satana amamuda Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yesu amalankhula zowona zenizeni.

-Satana anafuna kuti atsogoleri a Ayuda amuphe Yesu.

-Kodi chifukwa chiyani Satana anafuna kuti atsogoleri a Ayuda amuphe Yesu?
-Satana anafuna kuti atsogoleri a Ayuda amuphe Yesu kuti Iye asaŵapulumutse anthu.

-Satana anafuna kuti atsogoleri a Ayuda amuphe Yesu kuti Iye asawononge mphamvu ya tchimo ndi imfa.

-Satana anafuna kuti atsogoleri a Ayuda amuphe Yesu kuti Iye asawononge mphamvu yache.

-Chomcho, Yudasi anapita kwa atsogoleri a  Ayuda kukamupereka Yesu.

-Kodi aneneri analankhula kuti adzamupereke Yesu ndani?



Iye, akudya naye limodzi.

-Apanso Yesu ankafuna kuti Yudasi aganizire bwino za zimene ankafuna kuzichitazo.

-Kodi ndikulakwa kudyela pamodzi chakudya ndi munthu, koma mapeto ache ndikumupereka iye kwa adani?
-Inde.

-Ndikulakwa kwambiri.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:21

21-[Yesu anati] “Pakuti Mwana wa munthu amka ngati m’mene kwalembedwera za Iye. Koma tsoka kwa munthu amene akumupereka Mwana wa Munthu! Kukanakhala kwabwino kwa iye ngati sanakabadwa. “

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anadzitcha yekha kuti Mwana wa Munthu?
-Chifukwa chakuti Yesu analinso munthu weniweni.

-Chifukwa chakuti Yesu anadza ngati munthu kudzamupulumutsa munthu.

-Yesu anadziŵa kuti ayenera kufa.

-Koma ngakhale kuti Yesu anali oyenera kufa, munthu amene anakamupereka Yesu ankayenera kulandira chilango chachikuru kwambiri.

-Mulungu sanamukakamize Yudasi kuti amupereke Yesu.

-Yesu anadziŵa kuti Yudasi amupereka Iye.

-Kodi Yesu anadziŵa bwanji kuti Yudasi amupereka Iye?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu, Iye amadziŵa zinthu zonse.
-Palibe chimene Yesu sachidziŵa.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Yesu anaŵawuza ophunzira ache kuti m'modzi wa iwo amupereka Iye?
-Yesu ankafuna kuti Yudasi aganizire bwino za zimene iye ankafuna kuchita.

-Yesu ankafuna kuti Yudasi asinthe maganizo ache ndipo akabweze ndalama zimene iye analandira ndipo asamupereke Iye.

-Kodi kenako ophunzira a Yesu analankhula chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:19-20

19-[Ophunzira a Yesu] anali ndi chisoni, ndipo m'modzi m'modzi anati kwa Iye,"Kodi ndi ine?"
20-Yesu anayankha kuti, "Ndi m'modzi wa khumi ndi aŵiri, amene akususa m'bale imodzi ndi Ine."

-Chifukwa chakuti Yesu ndi ophunzira ache ankadyera pamodzi, Yesu analankhula kuti Iye aperekedwa ndi uyo amene akususa naye m'bale imodzi ndi Iye.

-Ayuda akamadyera pamodzi, amkanyemanyema mkate, ndi kumasusa m'bale imodzi ya ndiwo imene inkakhala pakati.

-Yesu analankhulanso kuti uyo amene adzamupereke



-Mzake.

-Ngati m'mene Mulungu analonjezera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, inafika nthaŵi yakuti Yesu aperekedwe ndi mzache.

-Kodi Yudasi atapita kwa akuluakulu a Ayuda kuti akamupereke Yesu, kodi akuluakulu a Ayuda ankaganiza chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:11

11-[Akuluakulu a msembe] anasangalala atamva izi ndipo anamulonjeza kuti adzamupatsa ndalama. Chomcho iye anafunafuna pomuperekera bwino Iye.

-Akuluakulu a Ayuda anamulonjeza Yudasi kuti amupatsa ndalama zokwana makumi atatu a siliva.

-Kodi nanga Yesu anaperekedwa pa ndalama zingati?
-Makumi atatu a siliva.

-Ngati m'mene Mulungu analonjezera kudzera mwa aneneri mu zaka zambiri zapitazo, Yesu anagulitsidwadi ndi ndalama zokwana makumi atatu a siliva.

-Kodi tsiku loyamba la phwando litafika, ophunzira a Yesu anamufunsa Iye chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:12

12-Ndipo pa tsiku loyamba la phwando la mikate yopanda chofufumitsira, pamene unali mwambo wawo wakupha mwana wa nkhosa, ophunzira a Yesu anamufunsa Iye kuti, "Kodi mukufuna kuti tikakonze kuti, kuti

mukadyereko Pasaka?"

-Ophunzira a Yesu anamufunsa Iye za kumene aka-
konze kuti akadyere phwando la Pasaka.

-Kodi phwando la Pasaka linali chiyani?
-Linali phwando limene Ayuda ankakumbukira zimene zinachitika ku Iguputo.

-Kodi chinachitika ndi chiyani ku Iguputo?
-Mulungu sanaphe ana awo amuna oyamba kubadwa, koma anaŵapitilira iwo chifukwa chakuti anapereka msembe ya mwana wa nkhosa ndikupaka magazi ache mphepete mwa chitseko.

-Apa pali zimene anaŵayankha Yesu ophunzira ache.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:13-15

13-Chomcho [Yesu] anaŵatuma ophunzira ache aŵiri, nati, "Lowani mu mzinda ndipo mukakumana naye munthu atasenza mtsuko wa madzi; mukamutsate iye.
14-Ndipo mukanene naye mwini wa nyumba imene iye akaloŵeyo kuti, "Mphunzitsi akufunsa kuti: Kodi chipinda cha alendo chili kuti, kumene Ine pamodzi ndi ophunzira anga tikadyereko Pasaka?"
15-Ndipo iye akakusonyezani chipinda chachikuru chapamwamba, choyaramo ndipo chokonzedwa bwino. Ndipo mukatikonzere m'menemo."

-Yesu anaŵawuza ophunzira ache kuti akakomana ndi munthu atanyamula mtsuko wa madzi, ndipo iwo akamutsate iye mpaka m'nyumba imene iye akaloŵemoyo.

-Ngakhale kuti ndi akazi okha amene ankanyamula



mitsuko ya madzi, Yesu anamudziŵa munthuyo.

-Yesu amadziŵa china chilichonse ndipo wina aliyense.
-Panalibe chinthu chimene sankachidziŵa Yesu.

-Muyenera kukhala m'nyumba m'mene munaloŵa munthuyo m'mene ophunzira a Yesu anakakonzamo kuti adyele phwando la Pasaka.

-Kodi mukuganiza kuti ophunzira a Yesu anakamupeza munthu atanyamuladi mtsuko wa madzi?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:16

16-Ophunzira achewo anapita mu mzinda, ndipo anakazipeza zinthu zili ngati m'mene Yesu anaŵawuzira. Chomcho iwo anakonzekera za Pasaka.

-Ophunzira a Yesu atatha kukhonzekera za phwando la Pasaka, madzulo atafika, Yesu pamodzi ndi ophunzira ache anapita ku nyumbayo .

Tiyeni tiŵerenge Maliko 14:17-18

17-Ndipo madzulo atafika, Yesu anadza ndi ophunzira ache khumi.
18-Iwo atakhala pa gome ndikumadya, [Yesu] anati, "Ine ndikukuwuzani zowona, m'modzi wa inu adzandipereka Ine – amene akudya nane."

-Kodi Yesu analankhula chiyani pamene Iye ankadya pamodzi ndi ophunzira ache?
-Yesu analankhula kuti m'modzi mwa ophunzira ache amupereka Iye.